




Boma la Malawi

KUTETEZA NKHUKU




KUMATENDA A CHITOPA

KATETEZEDWE KA MATENDA A CHITOPA

M'mene mungagwiritsire ntchito filipi tchatu

- Werengani zomwe mukufuna kukasonyeza ndipo muyetsere panokha musanafotokozere gulu.
- Muonetse chithunzi chilichonse mooneka bwino ndikuwafunsa alimi kuti afotokoze zomwe akuona.
- Onse akagwirizana ndi zomwe chithunzi chikusonyeza fotokozani zomwe chithunzi chikutanthauza.
- **DZIWANI:** Kufotokoza kwake kukuyamba motere:-
- Chithunzi choyamba



KUFUNIKA KWA ULIMI WA NKHUKU

Alimi amatha kupha zina mwa khuku zao kapena kuphika mazira ndikugwiritsa ntchito ngati ndiwo pakhomo pawo. Komanso ulimi wankhuku ndi imodzi mwa injira zomwe alimi amapezera ndalama, akagulitsa nkhuku zao kapena mazira mdziko muno. Zitosi zankhuku zimagwiritsidwa ntchito ngati manyowa makamaka pa ulimi wachimanga. Mudzi lathu lino pafupifupi alimi asanu ndi awiri mwa alimi khumi amaweta khuku.

Nkhuku zimachulukana msanga chifukwa sizichedwa kukula, komanso sizivuta kusamala. Aliyense pabanja amatha kukhala ndi nkuhu zachezache.

Nkhuku zimatipatsa nyama ndi mazira. Tikadya nyama ya nkhuku kapena mazira zimatithandiza kukhala moyo wathanzi. Khunku ndi mazira zikagulitsidwa zimabweretsa ndalama pakhomo kuti tipeze zosowa zathu. Zosowa zathu zikakhala zosalira ndalama zambiri, monga mankhwala kapena mabuku olembamo ana asukulu, chimakhala chinthu chapafupi kugulitsa nkhuku ndikusiyana kugulitsa mbuzi kapena ng'ombe.

Nkhuku zimanthanso kugwiritsidwa ntchito pa miyamb yosiyana-siyana, komanso ndiwo yake ndiyosavuta kukonza pakhomo pakabwera alendo mwadzidzidzi.

Choncho ndikofunika kuti tikasamalire nkhuku zathu moyenerera. Lero tikambirana zam'mene tingatetezere khuku zathu kumatenda achitopa omwe amapha nkhuku zambiri kwathu kuno chaka ndi chaka.

Matenda a chitopa ndi oopsya kwa alimi a nkhuku padziko lonse lapansi. M'dziko lathu lino la Malawi, nkhuku zambiri zimafa kaamba ka matendawa.




ZIINDIKIRO ZA MATENDA ACHITOPA

Matenda achitopa ndi matenda oopysy kwa alimi a nkhuku dziko lonse lapansi. Ku Malawi kuno, matewa akupha nkhuku zambiri kumudzi ndi m'mizinda momwe.

- Dziwani kuti sichitopa chokha chomwe chimapha nkhuku. Pali matenda osiyanasiyana omwe amapha nkhuku, koma chitopa chokha chimapha nkhuku zambiri kusiyana ndi matenda ena pa nthawi yochepa.
- Choncho tiyenera kudziwa zizindikiro za matendawa.
- Matendawa amadziwika ndi mayina osiyanasiyana m'maiko komanso m'maboma.
- Nanga kwanu kuno matendawa amadziwika ndi dzina lotani?





NKHUKU YOVUVUMALA

Yang'anani chithunzi ichi. Mukuona chiyani?

- Mapiko amagwa pansi. Madela ena amati nkhuku yavala jekete
- Nthenga zimanyankhalala
- Nthawi zina mutu umatupa





CHITOSI CHAMADZIMADZI CHOBIRIWIRA

Fotokozani zomwe mukuona pa chithunzipa

Nkhuku zimatsegula m'mimba ndipo chitosi chake chimaoneka cha madzimadzi chobiriwira

Kutsegula m'mimba kumapangitsa nthenga pa malo otulukira zitosi kukhala zozungulira zonyowa ndi zauve.






KHOSI LOPINDIKA

- Chithunzichi chikuonetsa chiyani?
- Nkhuku ikusonyeza khosi lopindika ndi nthenga zonyankhalala
- Kawirikawiri nkhuku imavutika kupuma.






KUFA KWA NKHUKU ZAMBIRI NTHAWI IMODZI

- Chikuchitika ndi chiyani pano?
- Nkhuku zambiri zafa
- Ndi nthenda yanji ingaphe nkhuku zambiri chocnchi pa kanthawi kochepa?
- Chitopa chimapha nkhuku zambiri nthawi imodzi. Chimfine chambalame chingathenso kupha nkhuku zambiri, koma matenda amenewa kwathu kuno kukadalibe.







ZIWETO ZAMTUNDU WA MBALAME ZIMENE ZITHA KUFALITSA MATENDA ACHITOPA

Ndi ziweto zANJI tikuona apa?

- Pali nkhangha, nkhekundembo, bakha ndi nkunda
- Ziweto zimenezi zikhoza kufalitsa matenda a chitopa
- Nkhangha, nkhekundembo ndi nkunda zikhoza kudwala matendawa
- Abakha akukuakulu amatha kudwala matendawa koma safa, pamene tiana tabakha timadwala nthawi zina ndi kufa.
- Mukaona kuti abakha amisinkhu yosiyanasiyana akufa dwiwani kuti akufa ndi matenda ena osati chitopa.






M'MENE MATENDAWA AMAFALIKIRA

- Mungafotokoze zomwe mukuona pa chithunzipa?
- Pano tikuona chithunzi chomwe chikusonyeza njira zomwe matenda achitopa amafalikira.
- Pakatipa pali nkhuku yosadwala.
- Mozungulira nkhukuyo pali zinthu zosiyanasiyana
- Pamwamba pali nkhuku yotsegula m'mimba
- Kumanja kuli galu akudya nkhuku yakufa ndi chitopa.
- Mbali ina kuli mazira
- Kenaka galimoto
- Pali zotsalira za nkhuku yophedwa monga nthenga, mafupa ndi zamkati.
- Pomaliza tikuona bambo atangoyima.

Chitopa chimayamba ndi tizirombo ting'onoting'ono toseka ndi maso totcheda vailasi. Mwachisanzo matendawa angafalikire ku nkhuku zina kupyolera ku nkhuku zodwala, nsapato, mazira, galimoto, zam'mimba ndi zotsalira za nkhuku zodwala

- Muli ndi mafunso okhuzana ndi zojambula waona apazi?





PALIBE MANKHWALA ACHIKUDA OCHIRITSA MATENDA A CHITOPA

- Tikuona chiyani apa?
- Tikuona a mayi akudandaula, abambo anyamula lichero, ndipo mulicheroli mukuoneka muli mankhwala achikuda; pansi pali nkhuku yodwala.
- Munayamba mwagwiritsapo ntchito mankhwala a chikudawa? Kodi adagwira ntchito?
- Mukudziwapo ena mwamankhwala achikudawa?
- Mumapereka mankhwalawa nthawi yanji? Pamene nkhuku yadwala kale kapena isanadwale?






KODI NDITANI KUTI NDIHKALE NDI NKHUKU ZA MOYO WABWINO

Kodi chithunzichi chikuonetsa chiyani?

Tikuona mayi yemwe ali ndi nkhawa ndi nkhuku zake. Iye akusinkhasinkha kuti adziwe njira zomwe zingamuthandize kuti akhale ndi nkhuku zamoyo wabwino.





KATEMERA WA CHITOPA

- Tikuona chiyani pa chithunzipa?
- Chitopa chilibe mankhwala.
- Tipewe chitopa pozipatsa nkhuku katemera.
- Nkhuku zipatseni katemera patangotsala mwezi umodzi pa miyezi imene matendawa amayamba mdera lanulo.
- Temerani nkhuku zokhazo ziri ndi moyo wabwino.
- Nkhuku ikayamba kudwala sikoyenera kuipatsa katemera. Katemera popanda bvuto.
- Pali mitundu yosiyanasiyana ya katemera. Pakali pano tikugwiritsa ntchito katemera wa mtundu wa 1-2 amene akuoangidwa kwathu konkuno ku Malawi. Katemerayu akhoza kukhala mwezi wathunthu kunja kwa firiji osatha mphamvu. Katemerayu ndi wofunika kwambiri ku mudzi komwe kulibe firiji.





KATHIRIDWE KATEMERA M'MASO

- Tikuona chiyani pa chithunzipa?
- Tikuona manja anayi a wathu.
- Manja atatu agwira nkhuku.
- Dzanja limodzi likudontheza katemera m'diso.
- Njira yabwino yotemera nkhuku ndi kudontheza katemera m'maso.
- Njirayi ndiyosavuta kuyiphunzira alimi.
- Nkhuku zamisinkhu yosiyanasiyana zipatsidwe dontho limodzi la katemera m'maso.
- Yang'ananso pa chithunzipa. Mutha kuona kuti botolo lodonthetsera katemera m'maso lagwiridwa molunjika ndi diso. Ndibwino kugwira botololi motero kuti muthe kudontheza katemerayu moyenerera.
- Muthanso kuona kuti pali manja a anthu awiri. Munthu m'modzi wagwira nkhuku pamene wina akupereka katemera.



NDONDOMEKO YA KATEMERA WA CHITOPA WA I-2



Temerani nkuku zanu kamozi pamiezi inayi iriyonse
Pogwiritsa ntchito katemera wachitopa wa I-2




nchito yomwe yakwaniritsidwa


Miyezi yolembera nkhuku	Miyezi yokonzekera kampani	Miyezi yotemera nkhuku	Miyezi younika zotsatira za kampani
<p>JANYUWA <input type="checkbox"/></p> <p>S M T W T F S</p> <p>1 2 3 4</p> <p>5 6 7 8 9 10 11</p> <p>12 13 14 15 16 17 18</p> <p>19 20 21 22 23 24 25</p> <p>26 27 28 29 30 31</p>	<p>FEBUL UWARI <input type="checkbox"/></p> <p>S M T W T F S</p> <p>1</p> <p>2 3 4 5 6 7 8</p> <p>9 10 11 12 13 14 15</p> <p>16 17 18 19 20 21 22</p> <p>23 24 25 26 27 28</p>	<p>MALICHI <input type="checkbox"/></p> <p>S M T W T F S</p> <p>1</p> <p>2 3 4 5 6 7 8</p> <p>9 10 11 12 13 14 15</p> <p>16 17 18 19 20 21 22</p> <p>23 24 25 26 27 28 29</p> <p>30 31</p>	<p>EPULO <input type="checkbox"/></p> <p>S M T W T F S</p> <p>1 2 3 4 5</p> <p>6 7 8 9 10 11 12</p> <p>13 14 15 16 17 18 19</p> <p>20 21 22 23 24 25 26</p> <p>27 28 29 30</p>
<p>MEYI <input type="checkbox"/></p> <p>S M T W T F S</p> <p>1 2 3 1 2 3 4 5</p> <p>4 5 6 7 8 9 10</p> <p>11 12 13 14 15 16 17</p> <p>18 19 20 21 22 23 24</p> <p>25 26 27 28 29 30 31</p>	<p>JUNI <input type="checkbox"/></p> <p>S M T W T F S</p> <p>6 7</p> <p>8 9 10 11 12 13 14</p> <p>15 16 17 18 19 20 21</p> <p>22 23 24 25 26 27 28</p> <p>29 30</p>	<p>JULAYE <input type="checkbox"/></p> <p>S M T W T F S</p> <p>1 2 3 4 5</p> <p>6 7 8 9 10 11 12</p> <p>13 14 15 16 17 18 19</p> <p>20 21 22 23 24 25 26</p> <p>27 28 29 30 31</p>	<p>OGASITI <input type="checkbox"/></p> <p>S M T W T F S</p> <p>1 2</p> <p>3 4 5 6 7 8 9</p> <p>10 11 12 13 14 15 16</p> <p>17 18 19 20 21 22 23</p> <p>24 25 26 27 28 29 30</p> <p>31</p>
<p>SEPITEMBALA <input type="checkbox"/></p> <p>S M T W T F S</p> <p>1 2 3 4 5 6</p> <p>7 8 9 10 11 12 13</p> <p>14 15 16 17 18 19 20</p> <p>21 22 23 24 25 26 27</p> <p>28 29 30</p>	<p>OKOTOBALA <input type="checkbox"/></p> <p>S M T W T F S</p> <p>1 2 3 4</p> <p>5 6 7 8 9 10 11</p> <p>12 13 14 15 16 17 18</p> <p>19 20 21 22 23 24 25</p> <p>26 27 28 29 30 31</p>	<p>NOVEMBALA <input type="checkbox"/></p> <p>S M T W T F S</p> <p>1</p> <p>2 3 4 5 6 7 8</p> <p>9 10 11 12 13 14 15</p> <p>16 17 18 19 20 21 22</p> <p>23 24 25 26 27 28 29</p> <p>30</p>	<p>DISEMBALA <input type="checkbox"/></p> <p>S M T W T F S</p> <p>1 2 3 4 5 6</p> <p>7 8 9 10 11 12 13</p> <p>14 15 16 17 18 19 20</p> <p>21 22 23 24 25 26 27</p> <p>28 29 30 31</p>

NDONDOMEKO YA KATEMERA WA CHITOPA WA I-2

- Mukuona chiyani pano?
- Tili ndi kalendala yomwe ili ndi malangizo. Kalendalayi ikusonyeza miyezi ya Malichi, Julayi ndi Novembala yomwe ikuoneka yoderapo. Iyi ndi miyezi yoyenera kupereka katemela. Choncho nkhuku ziyenera kulandira katemera kamodzi pa miyezi inayi iliyonse.
- Tikamatemera miyezi inayi iliyonse, nkhuku zizikhala ndi chitetezo chokwanira chaka chonse. Anapiye azikhalanso ndi chitetezo.
- Tionetsetse kuti tili ndi katemera wokwanira. Tiwerenge nkhuku ndikuyitanitsa katemera mofanana ndi chiwerengero cha nkhuku kampeni yisanayambe.



2





1

KASUNGUDWE KA KATEMERA

Ngakhale tinanena kuti katemerayu akhoza kusungidwa kwa mwezi popanda firinji, sikutanthauza kuti tisamusamale.

- Tikuona chiyani pa chithunzipa tikuona kuti katemera anayikidwa pa dzuwa. Katemera ameneyu ataperekedwa ku nkhuku, nkhuku sizinatetezedwe ndipo zinadwala.
- Nkofunika kusunga katemerayu pa malo ozizira ndi pouma bwino. Tisayike katemera pa malo otentha kapena pa dzuwa.
- Tikhoza kusunga pa m'tsuko wa madzi kapena kumukulunga mu nsalu yonyowa. Ikani katemera pa malo pamene pali mthunzi monga mukuona chithunzi chili pansichi.
- Pokatemera nkhuku ku midzi tengani katemera m'basiketi yachivindikiro, mutakulunga mu nsalu yopangidwa kuchokera ku thonje yonyowa.
- Kumbukirani kutemera nkhuku pa mthunzi.





MUSAGULE NKHUKU KUCHOKERA KU MIDZI YOMWE KULI CHITOPA

- Tikuona chiyani pano?
- Tsopano tikambirane za kapewedwe kofalitsa matendawa kuchokera mudzi wina kupita mudzi wina.
- Pachithunzipa amayi anagula nkhuku ku msika kupita nayo ku nyumba. Patapita masiku ochepa nkhuku zones zinafa.
- Tipewe kubweretsa nkhuku zina pa khoma tikaona kuti midzi yoyandikana nayo kwagwa chitopa.






CHOTSANI NKHUKU ZODWALA ZIKHALE PAZUKHA

- Ndiuzeni chomwe mukuona pa chithunzipa?
- Tikuona amayi ali ndi nkhuku komanso makola awiri a nkhuku.
- Akuchita chiyani?
- Akupatula nkhuku yodwala kuchokera ku khola lina lalikulu kupewa kufalitsa matenda ku nkhuku zina. Nkhuku ikadwala isapatsidwe katemera. Chomwe mungachite ndikuyipatsa chakudya, madzi ndikuyiyika malo abwino.
- Alimi ambiri amakhala ndi makola awiri. Kodi ndi alimi onse amene angakhale ndi makola awiri ankhuku?
- Mwina ayi. Mungachite chiyani posiyanitsa nkhuku zamoyo ndi zodwala.








KWIRIRANI NKHUKU ZOFA ZOKHA


- Chikuchitika pano ndi chiyani?
- Pamwambapo tikuona nkhuku zambiri zakufa.
- Mumachita chiyani nkhuku zambiri zikafa ndi chitopa?
- Nkhuku ikadwala ndi bwino kupha.
- Nkhuku zodwala kapena zakufa zisatengedwe kumudzi wina kumene kuli zamoyo.
- Nkhuku iliyonse imene yafa ikwiriridwe kapena itenthedwe.
- Chithunzi chapansichi amayi akukwirira nkhuku zakufa m'dzenje.
- Ngati nkhuku zafa ndi matenda achitopa musabweretse nkhuku zina m'deralo pasanathe masiku makumi atatu.






MAKOLA A BWINO


- Mukuona chiyani pano?
- Pali mitundu iwiri yamakola a nkhuku.
- Muli ndi khola la nkhuku pa khomo lanu? Ndilamtundu wanji?
- Khola labwino la nkhuku limathandizira kuteteza kufalitsa matenda.
- Nkhuku zikuluzikulu zikhoza kumagona khola la m'mwamba. Phaka la kholali lipangidwe la mitengo moti zitosi zizigwa pansu.
- Nkhuku za anapiye siziyenera kugona makola a m'mwamba. Ndi bwino zizigona makola apansi. Khomo lake lizikhala lalikulu loti munthu akhoza kulowamo ndi kusesamo.
- Nthawi zones chotsani makungwa amitengo kuopa kuti mungamabisale tizirombo monga utitili ndi nthata.
- Sesani m'khola la nkhuku kamodzi pa sabata. Ndipo mukamaliza kusesa wazani phulusa muzipupa mose kuti muthetse vuto la tizirombo tija.





KADYETSEDWE KA NKHUKU KOYENERA

- Mukuona chiyani pa chithunzipa
- Nkhuku zakumudzi kawirikawiri zimadzipezera zakudya zokha.
- Tikazipatsa chakudya choonjezera zimapereka phindu lochuluka.
- Nkhuku zodya bwino zimatetezedwa kumatenda ndi kulandira chitetezo chokwanira chakatamera.
- Chakudya chabwino ndichofunikanso kwa anapiye.
- Kodi anapiye tingawapatse bwanji chakudya chochuluka?
- Tingawapatse zakudya zotsala, misere yampungu, misere ya chimanga, masamba obiriwira, ziwala ndi zikokombe zosinja. Apatseninso madzi abwino.
- Chithunzichi chikusonyeza m'mene tingaperekere chakudya kwa anapiye okha. Apa zikusonyeza kuti ngati muli ndi chakudya chochepa mukhoza kupatsa anapiye okha osati zikuluzikulu.





KODI MULI NDI MAFUNSO?

- Chikuchitika ndi chiyani pano?
- Pali amayi awiri omwe akukambirana. M'modzi mwa amayiwa ali ndi nkhuku yodwala m'manja.
- Tikudziwa kuti chitopa simatenda okhawo omwe angaphe nkhuku zathu.
- Ngati muli ndi mavuto nthawi zones funsani alangizi anu omwe angakuthandizeni.
- Apa ndi pamapeto pazomwe tinakubweretserani. Ngati muli ndi mafunso kapena ndemanga ndili wachimwemwe ndi wosangalala kucheza nanu.



MAU OTHOKOZA

Tikufuna kuthokoza bungwe la Australian Centre for Agriculture Research, bungwe la National Veterinary Research Institute ku Mozambique, alimi ndi onse omwe anatengapo mbali pokonza bukhuli.

Bukhuli lakonzedwa ndi upangiri wa bungwe la Rural Poultry Centre (IRPC) yomwe ndi nthambi ya bungwe la KYEEMA Foundation ndi thandizo la ndalama lochokera ku bungwe la AusAID.

Kuti mudziwe zambiri fufuzani pa webusayiti iyi:
<http://www.kyeemafoundation.org/irpc.php>
(International Rural Poultry Centre)

kapena kafunsi ku:

Central Veterinary Laboratory
Vaccine Production Unit
P.O. Box 527, Lilongwe